***********************************************************

MAYANKHO.

3. Ayi. Inde.
5. Inde, adzatero. Ngati mumati ayi, werenganinso ndimeyo pa Luka.
1. Tidzazikambira m'kalasi zimenezi
7. Tikhoza kulilira kwa Mulungu kuti alimbikitse chikhulupiriro chathu.
2. Inde.
4. Yesu.
6. Analira, "Thandizani kusakhulupirira kwanga."

SABATA LACHISANU NDI CHIWIRI: KUKULA M'CHIKHULUPIRIRO
TSIKU LACHISANU:

Kodi sabata ino taphunzira zotani zoonjezera chikhulupiriro chathu? Taphunzira kuti tikhoza:-

1. Kukumbukira malonjezo a Mulungu.
2. Kuganizira mmene Iye anayankhira mapemphero a anthu ena.
3. kumpempha Mulungu kuti afunefune tchimo m'mitima mwathu.
4. Kumpempha Mulungu kuti aonjezere chikhulupiriro chathu.

1. Kodi Yesu anachita chiyani kwa munthu amene analira nati, "Thandizani kusakhulupirira kwanga"?

____________

____________________________________________

==========================================================

Pamene ophunzira anapempha Yesu kuti aonjezere chikhulupiriro chawo, sitiwerenga kuti Iye anawapatsa chikhulupiriro chambiri, koma m'malo mwake, Iye anasonyeza kuti ngakhale chikhulupiriro chaching'ono chikhoza kuchita zodabwitsa.

Luka 17:6:

Koma Ambuye anati, "Mukakhala nacho chikhulupiriro ngati kambewu ka mpiru, mukanena kwa mtengo uwu wamkuyu, "Uzulidwe, nuokedwe m'nyanja; ndipo ukadamvera inu."

2. Kodi Yesu anati kuti chikhulupiriro chathu chingafanane ndi chiyani?

________________________________

==========================================================

Kodi mbewu ndi chinthu chachikulu? Ayi, mbewu ya mpiru ndiyaing'ono kwambiri. Mwina mwake mumaona ngati kuti chikhulupiriro chanu n'chaching'ono kwambiri. Mwina mwake nthaŵi

zina mumanena kuti, "Sindingapempherere zinthu chifukwa chikhulupiriro changa sichili chokwanira." Yesu sanauze ophunzira ake kuti adikire mpaka chikhulupiriro chawo chitaonjezereka ayi. Iye anati ngakhale chikhulupiriro chawo chinali chaching'ono monga mbewu, koma ayenera kuchigwiritsabe ntchito.

3. Kodi muli ndi chikhulupiriro chachikulu kapena chaching'ono?

______________________________

==========================================================

Ngati muli ndi chikhulupiriro ngati mbewu, ndiye yambani kupempherera zinthu zazing'onozing'ono zimene zingakuthandizeni kuti mukhulupirire Mulungu. Tiyeni tinene kuti muli kupempherera wina wake m'banja lanu kuti akhale Mkhristu. Osangoyamba nkupemphera kuti munthu ameneyu atembenuke mtima maŵa. Yambani ndi kupemphera kuti Mulungu akuthandizeni kuti mumusonyeze chikondi chanu. Mulungu adzayankha pemphero lanu. Kenaka mumupemphe Mulungu kuti akupatseni mpata wakuti mukalankhule naye pa nkhani za zinthu za uzimu. Pambuyo pake mumupemphe Mulungu amuthandize kuti avomere kupemphera naye pamodzi ndi kuwerenga Buku Lopatulika.
naye.

4. Kodi muli nacho chikhulupiriro chokwanira cha kumpempha Mulungu kuti akupatseni mpata wokalankhula ndi mnzanu m'njira yomwe inu mungasonyezere chikondi chanu?

______

==========================================================

Pamene Mulungu ayankha mapemphero anu pa kanthu kakang'ono kondwerani kuti wakuyankhani. M'thokozeni chifukwa cha mphotho ya chikhulupiriro chanu chochepa. Kumbukirani kuti chinali chifukwa cha chikhulupiriro chanu, ngakhale ~~kuti~~ chinali chaching'ono, kuti Mulungu akuyankheni.

5. Mulungu amayankha mapemphero athu chifukwa tili ndi

______________________________

==========================================================

Nthaŵi zina pamene Mulungu amayankha mapemphero athu timanyengedwa ndi kumaganiza kuti, "Chabwino, zikanachitika ngakhale ndikanaleka kupemphera." Tikamanena zoterezi sindiko kukhulupirira Mulungu. Kukamba kotere kumafoketsa chikhulupiriro chathu. Kumachotsa ulemelero wa Mulungu. Nthaŵi ina Yesu anachiritsa anthu khumi odwala khate. Anthu asanu ndi anayi mwa iwo, pamene anaona kuti anachiritsidwa, anangopitiriza ulendo wawo osabwereranso kumbuyo kudzamuthokoza Yesu pa zimene iye anaŵachitira. Tatsekulani Buku Lopatulika ndipo muwerenge nthano iyi pa Luka 17:12.19.

6. Kodi m'modzi wa anthu akhate aja anachita chiyani pamene anaona kuti anachiritsidwa?

______________________________

==================================================

7. Kodi ife tizichita chiyani pamene Mulungu ayankha mapemphero athu?

________________________________________

==================================================

Gwiritsani ntchito chikhulupiriro chimene muli nacho. Choyamba pemphani zinthu zazing'onozing'ono. Ndipo Mulungu adzakuyankhani. M'thokozeni. Mukatha kumuthokozako mpempheni zinthu zazikuluzikulu.

8. Kodi chimachitika ndi chiyani ku chikhulupiriro chanu pamene mwaona kuti Mulungu wakuyankhani pamphero lanu?

__________________________________________________

==================================================

9. Kodi tingachite chiyani ndi chikhulupiriro chimene chiri chaching'ono?

______________________________________

Sitiyenera kukhumudwitsidwa ngati tikuona kuti chikhulupiriro chathu ndi chaching'ono.

(1) Tikhoza kuweŵerenga malonjezo a Mulungu m'Buku Lopatulika.
(2) Tikhoza kukumbukira mmene anayankhira mapemphero a anthu ena.
(3) Tikhoza kupempha Mulungu kuti atisonyeze ngati mitima yathu ili yoyera.
(4) Tikhoza kupempha Mulungu kuti atithandize kusakhulupirira kwathu.
(5) Tikhoza kugwiritsa ntchito chikhulupiriro chimene tili nacho pa kupempha zinthu zazing'onozing'ono.

10. Werenganinso njira zisanuzi zimene zimakuza chikhulupiriro chathu. Muziphimbe ndipo muphunzire kuzinena pa mtima osaonera.

***********************************************************

MAYANKHO

6. Iye anabwerera kudzamuthokoza Yesu.
3. Yankhani monga mungafunire.
1. Inde.
7. Tiyenera kumuthokoza.
4. Yankhani monga mungafunire.
2. Monga mbewu.
8. Ndikhulupirira kuti chikhulupiriro chanu chimakula ndi mphamvu.
10. Khalani okonzeka kunena m'kalasi.
5. Chikhulupiriro.
9. Tikhoza kuchigwiritsa ntchito.

SABATA LACHISANU NDI CHITATU: KUPEMPHERA NDI ANTHU ENA TSIKU LOYAMBA:

Kodi chikhulupiriro chanu ndi chotani mkupemphera? Kodi munali kupempha zinthu kwa Mulungu? Kodi mulikuyembekeza kuti akupatseni mayankho? Kodi mwakhala mulikuchita zinthu zokuza chikhulupiriro chanu?

1. Kodi chimene mwachita chokuza chikhulupiriro chanu ndi chiyani?

___

___

___

==========================================================

Pali chinthu chimene chimatithandiza kuti tizipemphera ndi chikhulupiriro. Takambapo kwambiri zakuti tizipemphera pa malo pa tokha. Yesu anati tizipita kumalo opanda phokoso ndipo kumeneko tiiwale zina zonse kenaka tiyambe kupemphera kwa Mulungu. Koma Yesu ananenanso kuti tiyenera kupemphera pamodzi ndi anthu ena. Ndime imodzi yogwira mtima yochokera m'Buku Lopatulika ndi iyi.

Mateyu 18:19.20:

> "Ndiponso ndinena kwa inu kuti ngati aŵiri a inu abvomerezana pansi pano chinthu chilichonse akachipempha, Atate wanga wa kumwamba adzawachitira. Pakuti kumene kuli aŵiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndili komweko pakati pawo."

2. Kodi wina ndani amene amakhala nawo pamene anthu aŵiri alikupemphera?

___

==========================================================

Pamene ife tikupemphera pa tokha Yesu nayenso ali pomwepo, koma Iye amadziŵa kuti zingatithandize ngati tikupemphera pamodzi ndi anthu ena. Iye amadziŵa kuti zingapangitse

chikhulupiriro chathu kukhala cha mphamvu pamene tikumva wina ali kupempherera zimene ife tili kupempherera. Choncho iye anatiuza kuti tizipemphera pamodzi ndi anthu ena, ndipo anatipatsa lonjezo lapadera la pemphero la mtundu umenewu.

3. Kodi Yesu analonjeza kuti ndi chiyani chingachitike ngati ife titabvomereza kupempherera pamodzi ndi anthu ena pa chinthu china chake?

__________________________________________________________

============================================================

Ndi m'Buku Lopatulika mmene timapeza chitsimikizo chakuti Mulungu amayankha mapemphero athu. M'Buku Lopatulika Mulungu anatiuza kuti ngati aŵiri a ife tigwirizana pa kupempherera chinthu china chake ndiye kuti chidzichitika. Tsekulani Buku Lopatulika ku Mateyu 18:19-20 ndipo werenganinso ndime zimenezi. Mutenge cholembera (pensulo) ndipo muzidula mizere ndimezo mmusi mwake.

4. Kodi Yesu anati nkwabwino kuti tizipemphera pamodzi ndi anthu ena?

____________________________________

============================================================

Werenganinso ndime izi monga mmene ndazilembera pano.

Mateyu 18:19-20:

"Ndiponso ndinena kwa inu kuti ngati aŵiri a inu abvomerezana pansi pano chinthu chilichonse akachipempha, Atate wanga wa kumwamba adzaŵachitira. Pakuti kumene kuli aŵiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndili komweko pakati pawo."

5. Bwerezaninso ndime izi mosalekeza, kapena kuti kaŵirikaŵiri mpaka mutaziloweza pa mtima. Ndakupatsani phunziro lachidule lero kuchitira kuti mupeze nthaŵi yoloŵezera ndime izi. Ndiyembekeza kuti mudzatha kuzinena m'kalasi pa mtima.

**********************************************************

MAYANKHO

5. Konzekani kunena ndime izi m'kalasi.
3. Iye ananena kuti chinthu chimenecho chidzachitidwa ndi Atate.
1. Tidzazikambira m'kalasi.
4. Inde.
2. Yesu.

SABATA LACHISANU NDI CHITATU: KUPEMPHERA NDI ANTHU ENA
TSIKU LACHIŴIRI:

Sabata ino tiphunzira zakupemphera pamodzi ndi anthu ena.

1. Kodi timadziŵa bwanji kuti kupemphera pamodzi ndi anthu M'Chipangano Chakale anthu a Mulungu anali kukumana pamodzi. Nthaŵi zina anali kumva Mawu a Mulungu. Nthaŵi zina anali kupereka nsembe kwa Mulungu. Nthaŵi zina kunali kwa mtsogoleri wawo, kapena Mose, kapena Yoswa, kapena Samueli, kapena Ezara, kuti awatsogolere m'mapemphero. Koma m'Chipangano Chatsopano munthu aliyense akhoza kupemphera molunjika kwa Mulungu.

2. Kodi anthu a m'Chipangano Chatsopano anali kupemphera m'dzina la ndani?

________________________________________

==========================================================

Nthaŵi zambiri timaŵerenga za m'mene Akhristu a m'Chipangano Chatsopano anali kupempherera pamodzi. Kupemphera pamodzi kunayambika pa mutu woyamba wa Machitidwe a Atumwi. Yesu anaŵauza kuti asachokemo mu mzinda wa Yerusalemu mpaka Mzimu Woyera atadza kwa iwo. Choncho iwo anakhala pamodzi alikuyembekezera zimenezi.

Machitidwe 1:14:

> Iwo onse anali kukangalika m'kupemphera pamodzi ndi akazi, ndi Mariya amayi wa Yesu, ndi abale ake omwe.

3. Kodi ophunzira anali kuchita chiyani pamene anali kuyembekeza Mzimu Woyera kuti abwere?

________________________

==========================================================

Sikunali kwakuti munthu m'modzi kapena aŵiri nkupempherera ena onse, koma onse anali kupempherera pamodzi nthaŵi zonse. Ŵerengani Machitidwe 2:1-4:

4. Kodi Mulungu anayankha bwanji mapemphero ogwirizana a anthu aŵa?

________________________________________

==========================================================

Zitatha izi, Akhristu anapitirizabe kupempherera pamodzi. Pa mutu wa 4 taona kale kuti Petro ndi Yohane anaŵaika m'ndende. Pamene akuluakulu anaŵatulutsa anaŵauza kuti asadzalalikirenso m'dzina la Yesu.

Machitidwe 4:23-24:

> Ndipo m'mene anamasulidwa, anadza kwa anzao a iwo okha, naŵauza zilizonse oweruza ndi akulu adanena nawo. Ndipo mmene anamva anakweza mawu kwa Mulungu ndi mtima umodzi, nati: "Mfumu, Inu ndinu wolenga thambo la kumwamba ndi dziko, ndi nyanja, ndi zonse zili mmenemo."

5. Kodi anthu ampingo anachitanji pamene anamva kuti analamulidwa kuti asalalikirenso m'dzina la Yesu mpaka muyaya?

________________________________________

==========================================================

Machitidwe 4:31:

> Ndipo mmene adapemphera iwo, panagwedezeka pamalo pamene adasonkhanirapo; ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nalankhula Mawu a Mulungu molimbika mtima.

6. Kodi Mulungu anamva pemphero lawo logwirizanalo?

________________________________

==========================================================

Pambuyo pake, Petro anali m'ndende ndipo taphunziranso m'mene mpingo unapempherera mosalekeza. Mulungu anatsekula zitseko za ndende ndipo mngelo anatsogolera mu msewu wa mu mzinda. Poyamba Petro anali wodabwa, koma kenaka anadziŵa chimene chinachitika.

Machitidwe 12:12:

Ndipo mmene adalingilirapo, anadza kunyumba ya Mariya amayi a Yohane wonenedwanso Marko; pamenepo ambiri adasonkhana pamodzi, ndipo anali kupemphera.

7. Kodi ndi anthu angati amene anali kupemphera m'nyumba imene analoŵa Petro?

______________________________

=========================================================

Pa Machitidwe 13, mpingo wa ku Antiokeya unaganiza zotumiza amishoni awo. Amishoniwo anali Paulo ndi Baranaba, amene anasankhidwa kuti apite pa ulendo wautali kukalalikira.

Machitidwe 13:3:

Pamenepo, mmene adasala chakudya ndi kupemphera ndi kuika manja pa iwo, anaŵatumiza amuke.

8. Kodi mpingo unachitanji kuti uŵatumize amishoni aŵa?

______________________________

=========================================================

Pa maulendo ake aumishoni zinthu zambiri zinamuonekera Paulo. Nthaŵi zambiri iye anali kupemphera ndi anthu ena. Pano pali zitsanzo ziŵiri zimene iye anapemphera ndi anthu ena.

Machitidwe 16:25:

Koma pakati pa usiku, Paulo ndi Sila analinkupemphera, nayimbira Mulungu nyimbo, ndipo am'ndendemo anali kuŵamva.

Machitidwe 21:5:

Ndipo kunali pamene tidatsiriza masikuŵa, tidachoka ndi kunka ulendo wathu, ndipo iwo wonse, akazi ndi ana anatiperekeza kufikira kutuluka m'mudzi; ndipo pogwadira pa m'chenga wakunyanja, tinapemphera.

9. Kodi chimene Paulo ndi Sila anachita akanali m'ndende ndi chiyani?

______________________________________________

==========================================================

10. Kodi Akhristu aku Turo anatsazikana naye bwanji Paulo?

______________________________________________

11. Kodi mpingo woyamba unali kuchita chiyani kaŵirikaŵiri?

______________________________________________

==========================================================

*******************************************************

MAYANKHO

8. Iwo anasala chakudya ndipo anapemphera naika manja pa iwo.
10. Anagwada pa m'chenga kunyanja ndipo ndikupemphera.
5. Anakumana pamodzi ndipo anapemphera.
3. Anapemphera.
11. Anapemphera pamodzi.
1. Buku Lopatulika limatiuza.
9. Anapemphera ndipo anaimba.
6. Inde.
4. Mulungu anaŵatumizira Mzimu Woyera.
2. M'dzina la Yesu.
7. Ambiri, kapena gulu lalikulu.

SABATA LACHISANU NDI CHITATU: KUPEMPHERA NDI ANTHU ENA TSIKU LACHITATU:

Dzulo tinaona mmene mpingo woyamba pa nthaŵi ya Atumwi unapezera mabvuto nthaŵi zambiri ndiponso unali kusoŵa zinthu zambiri. Pamene anthu a mpingo anaona zosoŵa zawo anakumana pamodzi.

1. Kodi mpingo unachita chiyani m'buku la Machitidwe pamene anakumana pamodzi?

____________________

==================================================

Pano pali phunziro kwa ife. Ife monga Akhristu, Mulungu amafuna kuti tizikumana pamodzi. Tisamangobwera ku tchalitchi kudzangoimba kapena kudzamva ulaliki chabe, koma tizibwera kudzapemphera pamodzi. Ndicho chimene inapangidwira nyumba ya Mulungu. Kodi mukukumbukira mmene Yesu anathamangitsira amalonda m'Kachisi wa Mulungu tsiku lina? Nthano imeneyi tikhoza kuiwerenga pa Luka 19:45-46:

Luka 19:45-46:

> Ndipo analoŵa m'Kachisi, nayamba kutulutsa ogulitsa malonda nanena nawo, "Kwalembedwa, "Ndipo nyumba yanga idzakhala nyumba yakupemphera, koma inu mwaiyesa iyo phanga la a chifwamba."

2. Kodi tchalitchi chanu ndi nyumba ya mapemphero? ____________

   Nanga mumatha nthaŵi yotani mukupemphera, nthaŵi yaitali kapena yochepa?

   ____________________

==================================================

Sindikunena kuti tizikhala ndi mapemphero aatali nthaŵi zonse pamene tibwera ku tchalitchi ayi. Nthaŵi zina pamene munthu wina apemphera pemphero lalitali kwambiri, iyi imakhala njira yosonyezera kuti anthu adziŵe momwe iye amalidziŵira Buku Lopatulika, kapena zinthu zimene angathe kuzi-

ganiza zabwino.

3. Chimachitika ndi chiyani kwa anthu ena ngati munthu wina apemphera pemphero lalitali?

________________________________

________________________________

==========================================================

Panthaŵi imene Yesu anali padziko lino lapansi, atsogoleri ena a Chiyuda anali kupemphera mapemphero aatali ndipo amangofuna kudzionetsera kuti anali abwino. Taonani zimene Yesu ananena kwa iwo.

Marko 12:40:
Amenewo alusira nyumba za akazi amasiye, napemphera monyenga mawu ambiri; ameneŵa adzalandira kulanga koposa.

4. Kodi chimene adzalandire atsogoleri a Chiyudaŵa ndi chiyani pamene amadziyerekeza kukhala abwino?

________________________________

==========================================================

Yesu sanali kunyoza mapemphero ameneŵa chifukwa chakuti anali aatali ayi, koma chifukwa chakuti anali onama. Yesu nayenso anali kupemphera nthaŵi yaitali. Nthaŵi zina iye anali kupemphera usiku wonse koma anali yekha. Pamene tipempherera pamodzi pa msonkhano, cholinga chake ndi chakuti aliyense apemphere. Kumbukirani kuti Yesu anati mu pemphero logwirizana muli mphamvu.

5. Kodi ili ndi pemphero logwirizana lakuti wina azipemphera pemphero lalitali, pamene ena alikungoganizira zawo?

________________________________

==========================================================

Mwina mwake mumadabwa mukamaona munthu m'modzi alikupemphera mokweza mawu. Kodi ndi chifukwa chiyani aliyense sangopemphera mmene angafunire pa nthaŵi imeneyi? Cholinga ndi chakuti munthu mmodzi ndiye ayenera kupemphera mokweza mawu chifukwa chakuti ndiye wotsogolera anzake mmapempheromo. Pamene munthu mmodzi alikupemphera, aliyense azingokhala alikuganizira za mawu amene alikunenedwawo. Iwo ayenera kupempherera chinthu chimenecho motsimikizadi m'mitima mwawo.

6. Ngati Mulungu amalonjeza kuti adzapatsa anthu aŵiri chinthu chimene agwirizana kuti achipempherere pamodzi, kodi muganiza kuti chingachitikedi n'chiyani ngati anthu makumi aŵiri kapena makumi atatu m'tchalitchi anagwirizana kupempherera chinthu china chake?

________________

____________________________________________________

============================================================

Kodi munthu amene alikupemphera m'tchalitchi angathe kutsogolera bwanji anzake? Choyamba ayenera kumanena mokweza kuti ena amvere.

7. Kodi anthu ena angapempherere chinthu monga chimene inu muli kupempherera ngati iwo sakumva zimene inu mulikunena?

_______________________________

============================================================

Munthu amene alikutsogolera pemphero ayenera kupemphera zinthu zenizeni zokhudza m'miyoyo ya anthu amene ali m'tchalitchimo.

8. Kodi ine ndingathe kupemphera nanu ndi mtima wonse ngati inu mulalikira pamene muli kupemphera?

________________

============================================================

Kodi anthu ena azichita chiyani pamene wina ali kupemphera? Asayang'ane uku ndi uko kapena kumaganiza zinthu zina, kapana kungoyembekeza kuti pemphero lithe, koma iwo ayenera kumapempheranso cha mumtima mwawo.

9. Kodi pamene wina alikupemphera m'tchalitchi inu mumachita chiyani? Muyenera kusamalira kuti muyankhe zoona!

________________________________________________________

=================================================

Mapemphero a m'tchalitchi satanthauza kuti ndicho chinthu chimodzi chakuti tingachite kuti tikwaniritse nthaŵi. Pemphero la m'tchalitchi limatanthauza kuchita china chake. Nyumba ya Mulungu ndiyo nyumba ya mapemphero. Kupemphera m'tchalitchi ndiyo nthaŵi yathu yolankhula ndi Mulungu monga mwa gulu. Ndi nthaŵi yomutamanda Iye. Ndi nthaŵi yokhalira pamodzi ndi kugwirizana kupempha zinthu zimene ife tikusoŵa.

10. Kodi pemphero liyenera kukhala mbali yaikulu kapena yaing'ono ya mapemphero a m'tchalitchi?

____________________

=================================================

Kodi mumadziŵa kuti m'buku la Machitidwe mpingo sunalikungopemphera pa misonkhano yokha imene inali kukhala pa sabata iliyonse? Iwo anali ndi misonkhano yamapemphero yapadera imene anali kupempherera zofunika zapaderanso. Iwo anapemphera pamene anali kupempha Mzimu Woyera kuti adze. Iwo anapemphera pamene olamulira anaŵauza kuti asadzalalikirenso. Anapemphera pamene mmodzi wa akuluakulu awo anali m'ndende. Anapemphera pamene anali kutumiza amishoni. Nanga bwanji ife? Ifenso tiyenera kukhala ndi misonkhano yapadera ya mapemphero pamene pali zofunika, pamene mulaliki alikubwera kuti adzalalikire, kapena pamene pali kusamvana mumpingo. Mulungu amamva pemphero logwirizana ngati limeneli.

11. Ngati pali zofunika zazikulu, kodi tiyenera kumapemphera bwanji m'tchalitchi?

____________________________________________

____________________________________________

************************************************************

MAYANKHO

7. Ayi.
10. Mbali yaikulu.
4. Chilango choopsya koposa, kapena kulamulidwa mwankhaza.
1. Iwo anapemphera.
3. Anthu ena amaganiza zinthu zina, kapena amagona.
5. Ayi.
8. Ayi, sichinthu chakuti tingakhalire pamodzi kuchipempha.
11. Tiyenera kukumana ndi kupemphera.
2. Yankhani monga mmene mungafunire, koma nthaŵi zambiri pali nthaŵi yochepa imene amatha popemphera m'tchalichi.
9. Ndinu nokha amene mungathe kuyankha funso limeneli.
6. Ndiganiza kuti Mulungu adzaŵapatsa.

## SABATA LACHISANU NDI CHITATU: KUPEMPHERA NDI ANTHU ENA TSIKU LACHINAYI:

Anthu ena amaganiza kuti kupemphera ndi anthu ena m'tchalitchi basi, kwakwanira. Ndipo amaganizanso kuti ngati atenga banja lawo kamodzi pa sabata kupita ku tchalitchi ndiye kuti ali kuchita bwino ndipo adzakhala Akhristu amphamvu.

Koma kupemphera kamodzi pa sabata ndi anthu ku tchalitchi sikungaphunzitse konse mabanja athu kulankhula ndi Mulungu. Ana amakhalanso ndi maphunziro awo apadera a Sande Sukulu (Sunday School), koma kupemphera ndi kuphunzitsa kwenikweni kwa mapemphero kunakonzedwera akuluakulu, chifukwa chakuti ana sangathe kumvetsetsa bwino nthaŵi zonse ayi.

1. Mudzawapenyetsetse ana ena pakati pa mapemphero ndi nthaŵi yolalikira sabata lamaŵa. Mudzaone ngati anawo akumva, kapena ngati alikungoyang'ana uku ndi uko kupenya zinthu zina.

=====================================================================

Ku tchalitchi ndiko kumalo abwino kuphunzirirako kukhala Mkhristu, koma tchalitchicho sichingatenge malo akunyumba monga kumalo kophunzirirako zimenezi. Tsopano, popeza tili ndi sukulu zabwino ndi matchalitchi abwinonso, anthu ena amaganiza zolekerera aphunzitsi ndi atsogoleri ampingo kuti ndiwo ali ndi udindo wophunzitsira anawo ku sukulu ndi kutchalichiko osati iwo ayi. Koma kuteroku mkulakwa kwakukulu. Ngati anakubala sanaphunzitse ana awo asanayambe kupita ku sukulu ndiye kuti aphunzitsi sadzatha kuŵathandiza mokwanira anawo kapena kuti aphunzitsiwo adzakhala ndi ntchito yaikulu kwambiri pofuna kuthandiza anawo kuti azindikire bwino.

2. Kodi kuphunzitsa mwana kufunika kuziyambira kuti?

______________________________________________________

=====================================================================

Mwina inu mukamamvetsetsa zimenezi mumaunzanso ana anu kuti iwonso azipemphera kaŵirikaŵiri. Kodi anawo adzaphunzira kupemphera chifukwa chakuti mumaŵauza kuti azipemphera? Ayi, ana amaphunzira mwakuyesera kuchita zimene amaona ife tikuchita. Kodi munayamba mwaonapo kamwana kakakazi kakukuphunzira kusenza zinthu pamutu pake? Kodi izi ndi zimene kamaphunzira ku sukuluyi? Kodi izi ndi zimene kamaphunzira chifukwa chouzidwa ndi amayi ake? Ayi, ikoka kamaphunzira kakamaona amayi ake ali kuchita tero, ndipo iko kamayeseranso kuchita.

3. Talembani zina zake zimene ana amaphunzira pitiona ife tikuchita, kenaka iwo nkumayeseranso kuchita.

==========================================================

Umu ndimo m'mene zilili ndi kupemphera. Ana ayenera kumatimva pamene tikupemphera pa nyumba ndipo iwo ayenera kupatsidwa nthaŵi yakuti nawonso ayesere kupemphera mwa iwo okha. Tizikhala ndi nthaŵi ina tsiku lililonse ya mapemphero a banja lonse. Nthaŵi iyi sikuti ikhale yolalikira ayi, kapena kuti munthu wina apemphere chipemphero chachitali ayi. Imeneyi iyenera kukhala nthaŵi yoganizira za Mulungu pamodzi ndi kulankhula naye monga mwa gulu. Alekeni nawonso ana agwemo m'mapemphero. Alekeni asankhe nyimbo. Alekeni anawo aŵerenge ndime.

4. Kodi ana azirimbikitsidwa kulankhula nanu za Mulungu?

==========================================================

Ngati tiŵaleka ana kuti azilankhula nafe momasuka za Mulungu ndiye kuti chidzakhala chosabvuta kwa iwo kulankhula naye Mulungu. M'mapemphero abanja lonse tiyenera kuonetsetsa za zimene ife tikusoŵa ndi zosoŵanso za banja lonse. Ngati ana adzamvera anakubala awo alikupemphera mwa njira imeneyi nawonso adzayesera kupemphera m'njira yomweyo.

5. Kodi ana angaphunzire bwanji kupemphera bwino?

________________________________________________________

________________________________________________________

==========================================================

Kupemphera ndi banja lonse sikuphunzitsa ana kokha ayi. Koma kumachitanso chinthu china chake. Kumathandiza kuti banja liziyenda bwino. Tiyeni tinene kuti pa tsiku lina banja silinagwirizane bwino ayi. Tiyeni tinene kuti atate ndiwo amene anali ndi phunzo lotukwana akazi awo pamodzi ndi ana awo omwe moipitsitsa zedi. Pamene alikupemphera Mulungu anaŵasonyeza kuti ndi wochimwa abambowo. Iyi ndiyo nthaŵi yabwino kwa atatewo yakuti apepese kuti anachimwa kwambiri.

6. Kodi muganiza kuti bambo azipepesa akalankhula molakwira banja lake?

________________________________

==========================================================

Ichi ndi chinthu chobvuta kuchichita, koma ndi chinthu chabwino ngati tifuna kuti Mulungu amvere mapemphero athu. Anthu ena amaganiza kuti izi zingapangitse kuti ana asadzakulemekezeni koma chodziŵika ndi chakuti ulemu udzapitirirabe ngati iwo ataona kuti atate wawo akonza chimene analakwacho. Ana nawonso adzadziŵa kuti ichi ndicho chimene ayenera kuchita ngati iwo afuna kuti mapemphero awo aziyankhidwa.

7. Kodi Yesu anati tizichita chiyani ngati tikupita kukapemphera ndipo takumbukira kuti pali china cholakwika pakati pa ife ndi mnzathu?

____________________________

________________________________________________________

==========================================================

Kupemphera pamodzi ndi banja lonse kumapatsanso mphamvu ndi chikhulupiriro. Ngati banja likufuna kanthu kena likhoza kukumana pamodzi ndi kumpempha Mulungu pa nthaŵi imeneyi. Mapemphero akayankhidwa, banja likhoza kukambirana za momwe